JW.ORG™
Koperani nkhaniyi pa www.jw.org

Mose Anabadwira ku Iguputo

EKISODO CHAPUTALA 1 NDI 2

Sankhani zimene mukuona kuti n'zogwirizana ndi ana anu.
Mukambirane zinthuzo monga banja.

WERENGANI EKISODO CHAPUTALA 1 NDI 2

Kenako onani zithunzi zofotokoza nkhani ya m'Baibulo (pa Intaneti kapena papepala limene mwasindikiza), ndiyeno kambiranani mafunso amene ali kumapeto.

ZINTHU ZINA ZIMENE MUNGASINDIKIZE

ZITHUNZI

KONGOLETSANI NDI CHEKENI Werenganinso Ekisodo 2:1-10. Uzani ana ang'onoang'ono kuti atchule mayina a anthu atatu amene ajambulidwawo. Kenako auzeni kuti akongoletse chithunzicho ndi chekeni.



ZOTI MUCHITE POPHUNZIRA

MIBADWO Uzani ana okulirapo kuti alembe mayina a abale ake a Mose. Malemba amene aikidwawo angawathandize kupeza mayinawo.

SUNGANI KUTI MUZIKUMBUKIRA

KHADI LA MUNTHU WOTCHULIDWA M'BAIBULO Onani kuti munthuyo anali ndani. Funsani mafunso amene ali pakhadilo. Chitani masewera osangalatsa pogwiritsa ntchito makadi onse amene muli nawo. Masewerawo akhale otere: Munthu m'modzi azisankha khadi ndipo ena onse asaone khadilo. Kenako anthu ena a m'banjalo aziyesa kudziwa dzina la munthu amene ali pakhadilo pofunsa mafunso amene yankho lake lingakhale lakuti "inde" kapena "ayi." Mwachitsanzo, angafunse kuti: Kodi munthuyo ndi wamwamuna? Kodi anakhalako Yesu asanabadwe? Kodi ankatumikira Yehova? Makolo kapena ana ena okulirapo angathandize ana ang'onoang'ono ngati pakufunikira kutero.

Nkhani zimene zili patsamba lino mungazipeze pa jw.org. (Pitani pagawo lakuti ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA > ANA > ZOCHITA PA KULAMBIRA KWA PABANJA.)

www.jw.org © 2014 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania